


Msamaria Wacifundo



Mogwirizana ndi Uthenga wa Mulungu:
Luka 10:25-37

Cilankhulidwe: CiNyanja

Panali m'phunzitsi m'modzi wa malamulo a Mulungu ndi Yesu. Iye anafunsa: —Ndingacite ciani kuti ndi khale ndi moyo. Umene Mulungu apatsa.

Yesu anayankha: —Malamulo a Mulungu ati ciani?

Munthu wacilamulo ca Mulungu anati: —Konda Mulungu ndi mtima wako onse. Konda nzako monga udzikondera mwini.

Yesu anabvomereza.

Munthuyo anamufunsa: —Ndani m'zanga naye? Iye amayesa kuti ali munthu wabwino.

Ndipo Yesu anamphunzitsa ndi fanizo limodzi:

Panali munthu amene. Anali kucokera ku Yerusalemu. Kupita ku Yeriko. Pakati panjira anakumana ndi acifwamba. Anamugwira, anamumenya, anamubvula zobvala zonse. Anansiya ndi zironda zambiri. Iye anagwa pansi nakomoka. Munali m'mphepete mwanjira. Acifwamba anathawa. Anadutsa mpomwepo mtsogoleri wa nyumba ya Mulungu.

Anamuona munthuyo koma sanaime. Anadutsanso munthu wina wa nyumba ya Mulungu. Ndiponso sanaime.



Ndipo anadutsa Msamaria. Aisrayeli ndi Asamaria sanali okondana. (Motero sanali kuyankhulana). Iye sanali opemphera. Anamupeza munthu udja ndi zirona za mbiri. Msamaria anamva cisoni. Ndipo anaima. Anacotsa mankhwala mu thumba mwace. Iye anamutsuka zirona. Namunyamulira pa nyama yace.

Msamariayo anafika kunyumba ya alendo. Ndipo anapempha malo. Anapereka ndalama kwa anuwake nyumba. Msamariayo anati: Ndidzasiyanso ndalama za mankhwala yena.

Yesu anafunsa: —Ndani anakhala munthu wabwino. Kwa munthu, wobvulara ndi wacifwamba?

Mphunzitsi anayankha: —Udja amene anamva cifundo naima. Namutsuka zirona. Amene anamuthandiza kumusamalira.

Yesu anati: —Iwe wayankha bwino. Pita ukacite comweco kwa wanthu wena. Cita monga munthu wa ku Samaria.

Yesu anaphunzitsa kuti munthu onyozedwa ndiye anakhala opambana. Munthu amene anakonda nzace.

Mafunso

1) Pafanizopa iwe uli ngati yani?

-Wacifwamba

-Mtsogoleri wa nyumba ya Mulungu

-Kapena wina udja wa nyumba ya Mulungu

-Kapena Msamaria

2) Iwe unamuthandiza kale m'dani wako, cifukwa amafuna thandizo?

Ficha Técnica:

Título: Msamaria Wacifundo
(Bom Samaritano)
(The Good Samaritan)

Língua: Cinyanja

Artista: Mbanji Bawe Ernest

Primeira edição electrónica, 2010

Produzido por: Wycliffe SA
lidemo.net@gmail.com
C.P. 652
Nampula, Nampula
Moçambique

O utilizador pode copiar e distribuir a obra

